NYA_TTB_0915_20160930_script

**Danieli : 1:1**

**Mutu : Kuunika Chiyambi cha buku la Danieli.**

Ndipereka moni wa Kumwamba kwa inu wokondedwa anzanga apaulendo. Tiyeni lero tiyambe ndi mau apa 1 Petro 3:10, pamene akunena kuti, "Pakuti Iye wofuna kukonda moyo, ndi kuona masiku abwino, aletse lilime lake lisanene choipa, ndi milomo yake isalankhule chinyengo."

Lero tiyamba kusanthula buku la Danieli 1:1, limene lili m'Chipangano Chakale. M'menemu tiona nkhani ya Chiyambi cha bukuli, kugwa kwa ufumu wa Yuda ndi kuonongeka kwa Yerusalemu.

Buku la Danieli ndi buku limodzi lomwe ndi lokondweretsa kwambiri m'Baibulo, popeza ndilo buku limodzi la ulosi. Tsono ndi koyenera kunena kuti chiphunzitso cha ulosi ndichimene chili ndi gawo lalikulu m'Baibulo. Tikunena kuti ¼, kapena kuti gawo limodzi la magawo anayi a mabuku a m'Baibulo ndi aulosi, amene amanena za m'tsogolo. Ndiye tiyenera kudziwa kuti ulosi m'Baibulo umagawidwa pawiri; ulosi wokwaniritsidwa ndi

wosakwaniritsidwa.Koma m'buku la Danieli tipeza ulosi wochuluka umene unakwaniritsidwa.Tikunena kuti ulosi wochuluka umene uli m'buku la Danieli, unakwaniritsidwa m'buku la Chibvumbulutso.Koma tiyenera kudziwa kuti mutu waukulu muulosi wonse, ndi Ambuye wathu Yesu Kristu. Ndipo mitu ina, ikukhudza Israyeli, dziko la amitundu, zonyasa, satana, munthu wochimwa, nthawi ya chisautso chachikulu komanso ulosi wokhudza momwe dziko lino lidzathere. Ndiye tiyenera kudziwanso kuti mpingo ndiwo ulosi wina, koma nkhani ya mpingo siipezeka m'Chipangano Chakale, kotero kuti m'buku la Danieli, sitiipeza nkhaniyi.Kuonjezeraapa, palinso ulosi wina wokhudza ufumu, wa zaka chikwi ndi ulosi woona kunthawiyosayamba.

Tsono ine, ndimakhulupirira kuti palibe munthu amene angakhale ndi chidziwitso chokwanira cha Baibulo, ngati sangadziwe chiphunzitso cha ulosi. Mwanjira ina, tikunena kuti kusoweka kwa chiphunzitso cha ulosi, chadza ndi zotsatira zoopsa kwambiri. Tere pankhani imeneyi a Dr. Hodge, mkulu wotchuka pakatanthauzidwekamau a Mulungu, adanena kuti, "Phunziro la ulosi silingathekukambidwa bwino, ngati sipangakhale kafukufuku

wokwanira pa utumiki wonse wa ulosi m'Chipangano Chakale ndi m'Chipangano Chatsopano chomwe."Mwachisoni lero lino kuti alipo anthu ambiri, amene alibe chidziwitso chokwanira kuti amayesera kukamba za ulosi.

Tsono buku la Danieli ndilo lofunika kwambiri, koma ndilo lakhalalodedwa kwambiri ndi satana monganso buku la Yesaya.Kutsindika kunena kuti mabuku onsewa ndi wofunika kwambiri m'mau a Mulungu, kotero kuti wotsutsa Kristu, akhala akuikamo nzeru zawo zabodza.

Anthu azipembedzo zina akhala akunena kuti buku la Danieli analilemba m'nthawi ya Antiokasindi Makabean m'chaka cha 170 B.C. patapita zaka 400, Danieli atapita kale. Koma chinthu cholimbikitsa ndi chakuti Baibulo la Septuagint, limene ndi la chi Greek la Chipangano Chakale, linatanthauzidwaAntiokasi ndi Makabeankulibe, momwe mukupezeka buku la Danieli.

Tsono buku la Ezekieli linatsekedwa likuonetsa mbiri yoopsa ya kuonongeka kwamzinda wa Yerusalemu, koma chokondweretsa ndi chakuti bukuli linaonetsanso ulosi wa ulemerero wa mzindawu mu Ufumu ulimkudza. Tere, buku la Danieli ndilo likufotokonzapomwe

buku la Ezekieli linalekezera.Mukumbukira kuti buku la Ezekieli ndilomwe linafotokonza zomwe zinachitika ndi zomwe zidzachitika mtsogolomo, m'zaka zoyambirira za ukapolo wawo. Pamene Danieli ndiye akufotokonza zomwe zinachitika ndi zomwe zidzachitika m'masiku omalizaa ukapolo wawo.

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone kuti nthawi zina Mulungu amagwiritsa ntchito manja angapo, koma ili ntchito imodzi yomweyo. Ndikunena mau amenewa chifukwa chinali chinthu choperekachitonthozokwa akapolo, kuti anali ndi mneneri woyamba pakati pawo kenaka analinso ndi wina. Iyi, inali njira imodzi yofunakuwasonyezakutarikakwa chilango chawo, nthawi yomweyo kuwasonyeza kuti Mulungu sanawataye.

Tsono dzina lakuti Danieli ndilachiHebri, lomwe limatanthauza kuti "Chiweruzo cha Mulungu."Uyu, ndiye uja anapatsidwanso dzina la chi Tchadi lakuti, Belitsezara. Danieli anali wamtundu wa Yuda wochokera ku banja la chifumu. Ndipo pali chitsimikizo chakuti anabadwira mu Yerusalemu.Iyeyu, ndiye anatchuka chifukwa chakukhala ndi nzeru zochuluka, komanso woyenda m'moyo wachiyero.

Tsono pamene tisanthula moyo wake, tipeza kuti palibe chimene chinalembedwa za iye, pamene anali wamng'ono. Iye ali pamsinkhu wochepa, anagwidwa ukapolo m'chaka cha 606 B.C. ndi Nebukadneza mfumu ya Babulo, pagulu loyamba la a Yuda, m'chaka cha chinayi cha Yehoakimu. Ukapolo wake unafikira mpaka m'chaka choyamba cha ulamuliro wa mfumu Koresi, m'chaka cha 536 B.C. Taonani iyeyu, akutchulidwa pamodzi ndi anzake atatu, Hananiya, Miseke ndi Azariya, amene anasankhidwa kuti akaphunzitsidwechilankhulo cha ku Babulo ndi cholinga chakuti akatumikire m'nyumba yachifumu.

A Yuda ndiwo anali anthu wogwidwa ndi kutengedwa ukapolo ku Babulo.Ndiye mwina mwadabwa kale kuti panali cholinga chanji kuti akasankheanyamatawa?Yankho likunena kuti, akapolowaanalibe mtendere ndipo mwina anali ndi mtima wosafunakumvera, kotero kuti kusankha ena mwa anyamata awo, inali njira imodzi yofunakuwakondweretsa.Ichi, ndichifukwa chake Nebukadneza anasankha ena mwa anyamata amene anali wochokera kunyumba yachifumu ndi kuwaika m'nyumba yachifumunso kuti akhale ndi mwayi wopatsidwa chakudya ndi

maphunziro apamwamba.Apa, panali cholinga chofuna kuwaganizira anthuwa m'maudindo ena kuti akhonzekuyendetsanawoboma. Anthu amenewa ndiwo amayenera kugwiritsidwa ntchito pakufuna kupereka Uthenga kwa a Yuda.

Pachifukwa chimenechi, Danieli analandira maphunziro apamwamba a science ya ku Babulo, kulankhula ndi kulemba chilankhulo chawo.Koma izi, zinachitika pamene anali ataphunzitsidwa kale m'chilankhulo, m'chikhalidwe cha chiHebri ndi m'chipembedzo cha makolo ake.Iyeyu, anaphunzitsidwamolimba pa malamulo achipembedzo cha makolo ake. Koma pano yafika nthawi yoyesakulimbakwa chikhulupiriro chake, popeza anaphunzitsidwa kolimba m'malamulo achipembedzo pankhani yazakudya ndi zakumwa. Pano Danieli ndi anzakeapatsidwa mwayi wazakudya ndi zakumwa ndi kukhala m'moyo wachisangalalo.Koma Danieli pamodzi ndi anzake, atsimikiza kuti sayenera kudzidetsa ndi zakudya ndi zakumwa zomwe ndi zoperekedwa ku mafano.Kutanthauza kuti anyamata awa, akanadya ndi kumwa zimenezi, akanakhala wodetsedwa ndi kuononga thanzi lawo chifukwa cha malamulo achipembedzo

chawo.Pachifukwa chimenechi, Danieli ndi anzake anafunitsidwakusungamatupi awo amphamvu komanso osadetsedwapakukanakutengapo gawo pa zakudya ndi zakumwazi.Ndipo anapempha kuti awalole kudya ndi kumwa madzi wokha ndi kuwayang'anira ngati matupi awo sadzasintha.

Koma taonani kuti pakutha pa zaka zitatu, Danieli ndi anzake anayenerezedwa kuti alowe kunyumba yachifumu kuti akatumikirem'magawo oyenera.Tsono chinthu choyamba chomwe Danieli anachita atalowa kunyumba yachifumu ndiko kutanthauziramaloto ya mfumu Nebukadneza.Ndiye pamene anatanthauzira molondola, anakwezedwakumpando wina wapamwamba, umene unampatsa mwayi woyendetsanawochigawo china cha Babulo (Dan.2).

Patapitanso nthawi panapezeka kuti Danieli anatanthauziransomalotoachiwiri, momwe anaonetsa kuti kudzikweza kwa mfumu kudzamuchotsera nzeru ndi kuchotsedwa pampando napitakutchire kukakhala pamodzi ndi nyama. Koma pambuyo pake adzabwezeretsedwanso (Dan.4).

Wokondedwa anzanga apaulendo, ndifuna muone kuti katanthauzidwekamaloto awa ndi kufotokonza momveka bwino zotsatira za kudzikweza ndi kukhala ndi ufumu wamphamvu padziko lonse, zinaonetsa kukhala ndi chikondi, kumvera ndi kukhudzidwa kwambiri ndi moyo wa munthu. Kutsimikiza kuti Danieli anatsogoleredwa ndi choona pakumasuliramalotoa mfumu. Ndiye ndifuna muone kuti pamene anaona choipa chikugwera ufumu uwu, iye anadzitsitsanapemphera ndi kulapa machimo ake ndi cholinga chakuti tsoka lichotsedwe lomwe likanatsitsa kwambiri ufumu wa Babulo.

Ndiye mwa mbiri ya Danieli yonseyi, tikupeza kuti moyo wa Danieli ndi utumiki wake, unakhalaulalo wa zaka makumi asanu ndi awiri za ukapolo wawo. Koyambirirakwa bukuli anali mnyamata, ndipo likutsekedwa ali nkhalamba. Koma kudzera m'moyo wake pa Danieli 10:11, tikuona Mulungu akunyadira Danieli ndi mau a mngelo akuti, "Danieli, munthu wokondedwatu iwe, tazindikira mau ndirikunena ndi iwe, nukhalechiriri; pakuti ndatumidwakwa iwe tsopano." Tere, ndimau amenewa ndiri ndi chikhulupiriro

chonse kuti tsiku lina, ndikamuona Danieli muulemererowa Atate, m'Mwamba.

Tiyeno pano tione mau atatu amene amaonetsa moyo wa Danieli: Poyamba ndifuna muone kuti Danieli ndiye anali munthu wa cholinga pochita zinthu (Danieli 1:8; 6:10), monga tikumva kuti "Koma Danieli anatsimikiza mtima kuti asadzidetse ndi chakudya cha mfumu, kapena ndi vinyo amamwa; chifukwa chake anapemphamkuru wa adindoamloleasadzidetse." Nkhani iyi, ikuchoka pakuti mfumu analamula kuti anthu onse kuphatikizapoanyamata atatu aja, anayenera kudya chakudya chimodzi cha kunyumba yachifumu.Koma taonani kuti Danieli ndi anzake anaganiza kuti adzasungabe malamulo a Mose, kuti asadyechakudyacho- ndipo anasungadi chimenechi. Ichi, chikutsimikiza kuti Danieli anali munthu wa "cholinga," kotero kuti tiona nkhani imeneyi m'buku lonseli. Kutsimikiza kuti Danieli anali munthu amene anaima nji! kulankhula ndi kuchita mau a Mulungu. Kodi inu mumaimachotere pamau a Mulungu?

Ndiye tikunena kuti Mulungu azitikhulululukiraife, amene timadzitchula kuti ndi atumiki a Mulungu, pamene tilibe mtima

wopereka mauwo monga ali. Komabe ndikoyenera kuyamika atumiki ena amene amapereka mau a Mulungu momwe amaphatikizapo chiphunzitso cha ulosi.Ndikunena mau amenewa chifukwa chiphunzitso cha ulosi ndichimene chimayeretsa moyo wathu. Ichi, ndichimene akunena Yohane pa 1 Yohane 3:3, pamene akuti, "Ndipo yense wakukhala nacho chiyembekezo ichi, pa Iye, adzayeretsa yekha, monga Iyeyu ali Woyera."

Kachiwiri, tiona kuti Danieli anali kukhala m'moyo wapemphero (Dan.2:17-23; 6:10; 9:3-19; 10). Ndiye tikunenetsa kuti moyo wapemphero ndiwo moyo uja unamulowetsa Danieli m'dzenje la mikango ndipo Mulungu mwa chozizwa, anamupulumutsakumikango ija.

Kachitatu, Danieli anali munthu waulosi.Tere buku lakelilikugawidwam'magawo awiri; gawo loyambalikufotokonza mbiri (History), pamene gawo lotsiriza muli ulosi. Pachifukwa chimenechi tikupeza kuti Danieli 2, momwe muli maloto a Nebukadneza, Danieli 7, zirombo ndizo msanamira za ulosi wake ndi ulosi wa masabata makumi asanu ndi awiri Danieli 9, ndizo zikuthandizira kuti zonse zikhale m'malo mwake.

Tsono mau otsogolera bukuli ali pa Danieli 2:44, amene akuti, “Ndipo masiku a mafumu aja Mulungu wa Kumwamba adzaika ufumu wotisudzaononongeka ku nthawi zonse, ndi ulamuliro wake sudzasiyidwira mtundu wina wa anthu, koma udzaphwanya ndi kutha maufumu awo onse.” Kutanthauza kuti ili, ndi buku losonyeza ulamuliro wa Mulungu pazonse. Ndiye pamene ulosi ukuphatikizana ndi mbiri ya dziko, zikuonetsa kuti Mulungu ali ndi ulamuliro pa chipembedzo cha mafano, kunyoza, kudzikweza ndi mwano wa anthu amitundu.

Ndiye pamene tiwerenga Danieli 12:4, tipeza kuti ndiye amene akubweretsa pamodzi nkhani ya anthu amitundu (Luka 21:24), ndi nthawi yakuthayapansi pano (Danieli 8:17; 11:35, 40), yomwe ndi nthawi yachisautso chachikulu cha Israyeli. Zinthu zonsezi zidzachitika kufulumiza kukhazikitsidwa kwa ufumu wa Kristu pansi pano. Iyi, ndi nkhani yomwe ikunenedwa pa Danieli 12:4, pamene akunena kuti, “Koma iwe, Danieli tsekera mau awa, nukomere chizindikiro buku, mpaka nthawi ya chimariziro; ambiri adzathamangachauko ndi chauko, ndi chidziwitso chidzachuluka.”

Tsono ndikoyenera kunena kuti buku ili, limafotokonza za kayendetsedwekaBoma kupatula kuonetsa za uzimu, koma limaonetsa yemwe adzalamulira dzikoli. Ndiye pazonsezi, tipeza kuti buku la Danieli ndilo limatsegula mitu, kuti mau a Mulungu amveke bwino. Mukumbukira kuti Ambuye Yesu kuphiri la Azitona, anagwira mau a m'buku la Danieli. Komanso buku la Chibvumbulutso silingamveke bwino popanda buku ili.

Tiyeni tione mitu ikulu-ikulu yomwe ikupezeka m'bukuli;

**I. M'dima wa mbiri (History) ndi kuwala kwa ulosi, chapters 1-6**

A. Kutha kwa ufumu wa Yuda; kugwa kwa Yerusalemu; Danieli atengedwa ukapolo ku Babulo; ndi kutsimikiza mtima kwake kuchita choona pamaso pa Mulungu, chapter 1

B. Lotola mfumu Nebukadneza ndi kumasulira kwake, kokhudza maufumu anayi, chapter 2

C. Nebukadnezaalamulira onse alambirefano; anyamataachiHebriaponyedwam'ng'anjo yamoto, chapter 3

D. Loto la Nebukadneza la mtengo waukulu, chapter 4,

E. Kugwa kwa Babulo, chapter 5

F. MfumuDariyoalamulirakumulambira, chapter 6

**II. Kuwala kwa ulosi mumdima wa mbiri (History) ya dziko, chapters 7-12**

A. Masomphenya a zirombo zinayi, wokhudza maufumu anayi, chapter 7

B. Masomphenya a nkhosa ndi mbuzi ndi nyangayaying'ono, chapter 8

C. Masomphenya a masabata makumi asanu, okhudza Israeli, chapter 9

D. Masomphenya a Danieli wokhudza Israyeli m'tsogolo, chapters 10-12

**Danieli 1 Kugwa kwa Yuda ndi kuonongeka kwa Yerusalemu**

1. Chaka chachitatu cha Yehoakimu mfumu ya Yuda, Nebukadnezara, mfumu ya ku Babulo adadza ku Yerusalemu, naumangiramisasa ya nkhondo.

Pano tiyambe ndi mau akuti, Yehoakimu anakhazikitsidwa pa ufumu wa Yuda ndi Farao Neko, kuti alowe m'malo mwa m'bale wake, Yehoyahazi. Mafumu awiri oipa onsewa, anali ana a mfumu

Yosiya, amene anali mfumu yabwino, yoopa Mulungu, yomwe inatsogolerachitsitsimutso mu Yuda (2 Maf.23:31-37). Ndiye pamene tilondola mbiri ya Yehoakimu, tipeza kuti ndiye anali Eliakimu. Tsono mkuyambakwa ulamuliro wa Nebukadnezara, anayamba ndi kuthira nkhondo pa Yerusalemu m'chaka cha 606 B.C. Munkhondo imeneyi, Yerusalemu sanaonongeke, koma gulu loyamba la a Yuda linatengedwa ukapolo ndi kupita nalo ku Babulo.Tsono pakati pachigulu chimenechi, panali Danieli ndi anyamata anzake, atatu.

Tsono pamene Yehoakimu anafa, mwana wake Yehoakini anakhala pampando waufumu wake. Uyu, ndiye mfumu anaukira ulamuliro wa Nebukadnezara. Iyi, ndiyo nthawi yomwe Nebukadnezara m'chaka cha 598 B.C., anabweranso ndi kuononga Kachisi wa Mulungu, natentha mzinda wa Yerusalemu. Tsono nthawi iyinsonkuti mzinda wa Yerusalemu sunaononngeke wonse, koma mfumu, mayi wake, ndi zipangizo zonse za m'Kachisi wa Mulungu, zinatengedwa ku Babulo pamodzi ndi gulu linanso lalikulu la anthu. M'guluuili, ndimomwe mneneri Ezekieli anatengedwa pamodzi (2 Mafumu 24:6-16).

Pambuyo pa gulu ili, tikupeza kuti Zedekiya, tate wake wamng'ono wa Yehoakini,anakhazikitsidwa mfumu ya Yuda, amene anaukiranso Nebukadnezara. Apa, ndipo pamene Nebukadnezara anadzanso ndi mphamvu ndi kuthira nkhondo Yerusalemu, kuononga Kachisi wa Mulungu, ndi kutentha Yerusalemu. Ana a mfumu Zedekiya anaphedwa mfumu akuona, kenaka maso a Zedekiya anakolowoledwa, kotero kuti iye ndi gulu lomaliza, anatengedwa kuukapolo m'chaka cha 587 B.C. Ndiye tikunena kuti zinthu zonsezi zinali kuchitika potsatira ulosi wa Yeremiya 25:8-13.

Wokondedwa anzanga apaulendo, pamene tikutsiriza ndifuna tione kuti Yeremiya ndi Ezekieli ndiwo amene anauza anthu a Yuda kuukapolo kuja, kuti aneneri onama, anali kuwauzazabodza kuti Yerusalemu sadzaonongeka.Koma choona ndi chakuti, aneneri awiriwa ndiwo anali kunena zoona.

Kwalerotilekeza pano. Koma tinali kusanthula Danieli 1:1, momwe taona nkhani ya chiyambi cha bukuli, kugwa kwa ufumu wa Yuda ndi kuonongeka kwa mzinda wa Yerusalemu.

Ambuye akudalitseni inu. Amen!